-Koma aliyense odzikweza yekha pa maso pa Mulungu, Mulungu adzamutsitsa.



PHUNZIRO LA 58

1. Kodi chifukwa chiyani khamu la anthu lalikuru kwambiri linamulondola Yesu?
-Chifukwa chakuti ankAfarisiuna kuti adziwona zizindikiro zambiri zozizwitsa zimene Yesu ankaŵachitira anthu odwala.

2. Kodi anthuwo analipo angati?
-5,000.

3. Kodi pamene Yesu ankayamba kuŵapatsa chakudya anthu, anali ndi mikate ndi msomba zingati?
-Mikate isano ndi msomba ziŵiri.

4. Kodi Yesu anatha bwanji kuŵadyetsa anthu 5 000 ndi mikate isanu ndi msomba ziŵiri?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.
-Yesu akhoza kuchita china chilichose.

5. Kodi chifukwa chiyani anthu ankAfarisiuna kumudzodza Yesu ufumu?
-Chifukwa chakuti ankAfarisiuna kuti Iye adziŵapatsa chakudya nthaŵi iliyonse.

6. Kodi chifukwa chiyani Yesu sanAfarisiune kuti akhale Mfumu ya anthu?
-Chifukwa chakuti Yesu anadziŵa kuti mitima ya anthu inali yoyipa.
-Chifukwa chakuti Yesu anadziŵa kuti anthu ankAfarisiuna kuti Iye adzingoŵapatsa chakudya basi.

7. Kodi Yesu anAfarisianana bwanji ngati mana amene Mulungu Atate anapereka kwa a Isilayeli m’chipululu muja?

-Yesu anachokera kumwamba ngati m'mene anachokelera mana kumwamba.
-Yesu anaperekedwa ndi Mulungu ngati m'mene mana anaperekedweranso ndi Mulungu.
-Ngati m'mene a Isilayeli anakAfarisiera anakapanda kudya mana , chomchonso anthu adzAfarisia ngati sakukhulupilira mwa Yesu.

-Tsiku lina Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo anapita kukacheza ndi Yesu.

Tiyeni Tiŵerenge Maliko 7:1-5

1-Afarisi , pamodzi ndi aphunzitsi ena a malamulo, amene anachokera ku Yelusaremu, anasonkhana kwa Yesu.
2-Iwo anaŵawona ophunzira a Yesu akungodya chakudya m'manja mwawo muli moyipa, mosasamba.
3-Pakuti Afarisi ndi Ayuda ena onse sadya chakudya asanasambe bwinobwino m'manja mwawo, potsata miyambo ya makolo.
4-Pochokera ku msika asanadye china chilichonse, ankayamba asamba m'manja kaye, potsata miyambo ya makolo. Panalinso miyambo ina imene makolo awo anaŵasiyira ngati kutsuka mbiya, miphika ndi ziwiya.
5-Ndipo Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo aja anamufunsa Yesu kuti, "Kodi chifukwa chiyani ophunzira ako sakuyitsatira miyambo ya makolo athu, akungodya m'mamnja muli moyipa?"

-Kodi chifukwa chiyani Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo anakwiya ndi ophunzira a Yesu?
-Chifukwa chakuti ophunzira a Yesu sankasunga miyambo ya akuluakulu.



-Iye anamupenpha Mulungu kuti amupulumutse.

-Kodi nanga kenako Yesu anati chiyani?

Tiyeni Tiŵerenge Maliko 18:14

14-Yesu anapitiriza ndikuti, "Ndikukuwuzani zowona, munthu ameneyu anapita kwawo ali olungamika pa maso pa Mulungu kusiyana ndi Mfarisi uja; pakuti aliyense odzikweza adzamutsitsa, koma odzitsitsa adzamukweza.

-Kodi Mulungu anamulandira Mfarisi uja?
-Ayi.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamukana Mfarisi uja?
-Chifukwa chakuti iye sankakhulupilira kuti anali ndi mtima oyipa
-Chifukwa chakuti iye sankakhulupilira kuti anamuchimwira Mulungu.

-Kodi Mulungu anamulandira okhometsa msonkho uja?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulandira iye?
-Chifukwa chakuti iye anadziŵa kuti anali ndi mtima oyipa.
-Chifukwa chakuti iye anadziŵa kuti wamuchimwira Mulungu.

-Kodi pa mathero a fanizo limeneli, Yesu analankhula chiyani?
-Yesu analankhula kuti aliyense odzichepetsa yekha pa maso pa Mulungu, Mulungu adzamukweza.

-Chifukwa chakuti iye ankapereka chakhumi ku Nyumba ya Mulungu pa zonse zimene ankapeza.

-Mfarisiyu anali odzikweza kwambiri.
-Iye ankaganiza kuti anali munthu wabwino.
-Iye ankaganizanso kuti zonse zimene ankachita zinali zabwino.
-Iye ankaganizanso kuti anali bolani kuposa anthu ena.

-Iye sankakhulupilira kuti ankasoŵa Mpulumutsi.

-Kodi nanga bwanji okhometsa msonkho uja?

Tiyeni Tiŵerenge Maliko 18:13

13-“Koma okhometsa msonkho uja, anayima potalikirako, ndipo sanayerekeze zonyamula nkhope yache ndikuyang’ana kumwamba, koma modzichepetsa, anadzigogoda pa mtima pache, ndipo anati, “AMBUYE, ndichitireni ine chifundo, ochimwa !”

-Kodi okhometsa msonkho uja ankaganiza chiyani za iye mwini?
-Iye anadziŵa kuti mtima wache siwunali oyera.

-Kodi nanga iye anadziŵa bwanji kuti mtima wache siwunali oyera?
-Chifukwa chakuti iye ankadziŵa kuti maganizo ache oyipa nkachokera ku mtima wache onyansa.
-Iye ankadziŵa kuti anali ochimwa ndipo anamuchimwira Mulungu.

-Iye anadziŵa kuti sangathe kusintha kuyipa kwa mtima wache.
-Iye anadziŵa kuti ankayenera kufa.



-Kodi miyambo ya akuluakulu inali chiyani?
-Inali miyambo imene Afarisi anakhazikitsa imene ankati kuti anthu ayenera kumayitsatira kuti akalandiridwe ndi Mulungu.

-Kodi Mulungu amaŵalandila anthu chifukwa cha miyambo ya makolo imene amayisunga?
-Ayi.

-Chifukwa chakuti Afarisi ankasunga miyambo yonse imene anayikhazikitsa ankaganiza kuti Mulungu walandira kale.

-Ngakhale kuti Afarisi ankasunga miyambo yonse ya makolo, mitima yawo inali yoyipa.

-Kodi kusunga miyambo kungakuchititsèni inu kukhala wa mtima wabwino?
-Ayi.

-Ngakhale kuti Afarisi ankasunga miyambo yonse ya makolo panja pokha, mitima yawo inali yoyipa kwambiri nkati mwawo.

-Kodi ngati mphika wanu uli ndi chitosi mkati, zingakuthandizeni kungowutsuka panja pokha?
-Ayi.

-Kodi Yesu anaŵawuza chiyani Afarisi.

Tiyeni Tiŵerenge Maliko 7:6

6-Ndipo [Yesu] anaŵayankha kuti, “Yesaya analankhula kale kuti inu ndi odzikonda ngati m’mene

zalembedwera kuti, “Anthu aŵa akundipembedza Ine ndi pakamwa pawo pokha, koma mitima yawo ili kotalikilana ndi Ine. “

-Yesu anaŵanena Afarisi kuti ndi odzikonda.

-Kodi munthu odzikonda ndi munthu otani?
-Munthu odzikonda ndi munthu amene mawu ake ndi zochita zake zimakhala zosiyana.

-Ndipo Yesu analankhulanso kuti zimene zinalembedwa M’buku la Mulungu ndi Mneneri Yesaya za iwowo, zinali zowona.

-Kodi Mneneri Yesaya analankhula chiyani za anthu ameneŵa?
-Mneneri Yesaya analankhula kuti anthu ameneŵa amangolankhula ndi milomo yawo yokha kuti akumukhulupilira Mulungu, koma mitima yawo ili kotalikana ndi Mulungu.

-Mneneri Yesaya analankhula kuti iwowo ankamukhulupilira Mulungu ndi mawu awo okha , koma osati mitima yawo.

-Kodi Mulungu amaŵalandira anthu amene amamukhulupilira Iye ndi mawu awo okha?
-Ayi.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Yesu kwa Afarisi?

Tiyeni Tiŵerenge Maliko 7:7-9

7-[Yesu anati] “Kupembedza kwawo ndi kwacha-



-Maganizo oyipa, kugwilira, kuba, kupha, chigololo, umbombo, msanje, bodza, mwano, miseche, kudzikweza ndi kupusa.

-Kenako Yesu anaŵawuza fanizo anthu.

Tiyeni Tiŵerenge Maliko 18:9-12

9-Yesu analankhulanso fanizo ili kwa anthu ena amene ankadziwona ngati olungamika ndikumaŵanyoza anzawo:
10-anati kuti, “Panali anthu aŵiri amene anapita kukapemphera ku Nyumba ya Mulungu, wina anali Mfarisi ndipo wina anali okhometsa msonkho.
11-Mfarisiyo anayima payekha ndikuyamba kupemphera za iye mwini, ndikumati, “AMBUYE, ndikukuyamikani chifukwa chakuti ine sindili ngati anthu enaŵa, amene ali akuba, osalungamika, achigololo, komanso sindili ngati munthu okhometsa msonkhoyu.
12-Ine ndimasala kudya kaŵiri pa sabata iliyonse, ndiponso ndimapereka cha khumi cha zonse zimene ndimapata.”

-Kodi mu fanizolo, ndi ndani amene anapita ku Nyumba ya Mulungu kukapemphera?
-M’modzi anali Mfarisi ndipo wina anali okhometsa msonkho.

-Kodi Mfarisiyo ankaganiza chiyani za iye mwini?
-Mfarisiyo ankaganiza kuti mtima wache unali woyera.

-Kodi chifukwa chiyani Mfarisiyo ankaganiza kuti mtima wache unali oyera?
-Chifukwa chakuti iye ankasunga miyambo ya makolo.
-Chifukwa chakuti iye ankasala kudya kaŵiri pa sabata.

chingamupangitse munthu kukhala odetsedwa?
-Yesu analankhula kuti chimene chili mkati mwa munthu ndi chimene chingamupangitse munthuyo kukhala odetsedwa.

-Kodi chimene chili mkati mwa munthu chimene chingamupangitse munthuyo kukhala odetsedwa ndi chiyani?
-Mtima wache.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anachimwa m'munda wa Edeni, mitima yawo inadetsedwa.

-Kayini ndi Abele anabadwa ali ndi mitima yodetsedwa.

-Aburahamu, Isaki ndi Yakobo, anabadwa ndi mitima yodetsedwa.

-A Isilayeli onse anabadwa ndi mitima yodetsedwa.

-Anthu onse anabadwa ndipo akubadwa ndi mitima yodetsedwa.

-Chifukwa chakuti anthu onse akubadwa ndi mitima yodetsedwa, kudetsedwa kumachokera m'mitima yathu.

-Kodi Mulungu amakuwona kuyipa kumene kuli m'mitima mwathu?
-Inde.

-Mulungu amawona kuti mitima yathu yonse yadzadza ndi zoyipa.

-Kodi zoyipa zimene zili mkati mwa mtima wa munthu aliyense ndi zotani?



bechabe chifukwa chakuti amaphunzitsa malamulo opanga anthu ngati kuti iwowo ndi malamulo a Mulungu enieni."

8-Ndipo inu, mukuŵasiya malamulo a Mulungu, ndikumayigwiritsa tchito kwambiri miyambo ya anthu."

9-Yesu anapitirizabe ndi mawu ache akuti, "Muli ndi njira zodzikonda zosiyira malamulo a Mulungu mwadaladala kuti mudziyigwiritsa nthito miyambo ya anthu!"

-Yesu analankhula kuti Afarisi ankamupembedza Mulungu paderadera.

-Kodi Afarisi ankamupembedza bwanji Mulungu paderadera?
-Chifukwa chakuti Mulungu sankakulandira kupembedza kwawo.

-Chifukwa chiyani Mulungu sankakulandira kupembedza kwawo?
-Chifukwa chakuti kupembedza kwawo kunali kwa thupi lawo lokha osakhala kochokera m'mitima yawo.

-Kodi Afarisi ankachita chiyani potsata miyambo yawo?
-Ankaswa malamulo a Mulungu.

-Kodi Mulungu amafuna kuti anthu adziwonjezera miyambo yawo ku Buku Lache, Bayibulo?
-Ayi.

-Tisadzayelekeze kuwonjezera kapena kuchotsa china chilichonse chimene Mulungu walankhula M'bayibulo.

-Yesu atatha kulankhula zimenezi kwa Afarisi, analiyitana khamu la anthu lija.

## Tiyeni Tiŵerenge Maliko 7:14-15 ndi 17-19

14-Yesu analiyitananso khamu la anthu lija kuti libwere pAfarisiupi ndi Iye, ndipo analiwuza kuti, "Anthu inu mundimvetse ndiponso mudziŵe zimenezi.

15-Palibe chinthu chimene chimachokera kunja ndikulowâ m'mimba mwa munthu ndikumuyipitsa iye; koma chimene chikuchokera mkati mwa munthuyo ndi chimene chimamuyipitsa iye."

17-Atasiyana ndi anthu aja, analowâ m'nyumba, ndipo ophunzira ache anamupenpha kuti aŵatanthawuzire fanizo limeneli.

18-Iye anaŵAfarisiunsa kuti, "Kodi nanunso simukudziŵabe? Kodi simukudziŵa kuti chinthu chilichonse chimene chimachokera kunja , ndi kulowâ mwa munthu, sichitha kumuyipitsa munthuyo?

19-Pakuti sichikulowâ mu mtima mwache, koma m'mimba , ndipo pambuyo pache chimaturuka." (Polankhula zimenezi, Yesu analamula kuti zakudya zonse akhoza kumadya.)

-Kodi Yesu analankhula chiyani kwa khamu la anthu lija?
-Yesu analankhula kuti palibe chimene chingalowê mwa munthu kuchokera kunja chimene chingamudetse.

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani?

-Yesu ankatanthawuza kuti anthu sangadetsedwe ndi kusasamba m'manja kapena chakudya chosatsuka.

-Kodi chifukwa chiyani anthu sangadetsedwe ndi kusasamba m'manja kapena chakudya chosatsuka?
-Chifukwa chakuti zimenezi sizikhuza mtima.



-Yesu analankhulanso kuti zimenezi zimalowâ m'mimba ndikuturukanso m'thupi popanda kukhudza mtima.

-Kodi Mulungu angatilandire chifukwa cha zinthu zimene ife timadya?
-Ayi.

-Kodi Mulungu angatilandire chifukwa cha zinthu zimene ife sitimadya?
-Ayi.

-Kodi Mulungu angatilandire chifukwa cha zovara zimene ife timavara?
-Ayi.

-Kodi Mulungu angatilandire chifukwa cha zovara zimene ife sitivara?
-Ayi.

-Kodi china chiyani chimene Yesu analankhula?

## Tiyeni Tiŵerenge Maliko 7:20-23

20-Yesu anatinso, "Zimene zimaturuka mwa munthu ndi zimene zimamuyipitsa munthu.

21-Chifukwa chakuti mkati mwa mitima ya anthu ndi m'mene mumaturuka maganizo oyipa a, kugwilira, kuba, kuphana, chigololo

22-umbombo, kusilira, chinyengo, kunyansidwa, kuzonda, kudzikuza ndi kupusa.

23-Zoyipa zimenezi ndi zimene zimachokera mkati ndikumuyipitsa iye.

-Kodi Yesu analankhula kuti ndi chiyani chimene